anati :sindilowedwa m'malo ,ndiye anamuletsa Fatwimah (A.S)gawo lake lachuma kuchokera kwa bambo ake (S.A.W)''. (Qarbu Al Isnaad, lolembedwa ndi Humayiry Al Qummy (300 A.H), P.99— wosindikiza ndi kufufuza : ''Muassasattu Aal Al Bayt li-ihyaa-i Al Turaath,Edition yoyamba).Muriwaya lina ananena Allie Bun Abi Twalib kwa azimayi awiriwa kuti: ''munalibe wina aliyense mwa maswahaba a M'tumiki wa Allah (S.A.W) ; maswahaba osamuka (ma Muhajiroona) ngakhalenso oteteza (ma An-saar) amene anayikira umboni zimenezi posakhala inu awiri ndi ''Mu'arabiyu'' (Muluya wakumidzi) koma Wallahi ndilibe chikayiko china chilichonse kuti munthu ameneyu anamunamizira M'tumiki wa Allah (S.A.W),nanunso awirinu (Aishah ndi Hafsah) munamunamizira M'tumikiyo pamodzi ndi munthu ameneyu''. (Buku la Salimu Bun Qaysi, P.242).

Chachisanu ndi chitatu kunenetsa kwa m'modzi mwa Maulama akuluakulu a chishia zoti azimayi awanthu okhulupilira Aishah ndi Hafsah anali mamunafiqu omwe amabisa ukafiri wawo.

Mazindarany poyikira ndemanga hadithiyi anati: ndithu anali M'tumiki wa Allah (S.A.W) atakwatira '',anati zikutanthauza kuti anakwatira Aishah ndi Hafsah ndiye awiriwa anapanga za umunafiqu ndikubisa ukafiri ndi kusakhulupirika kwaiye (S.A.W) pazomwe anapangazi. (Sharhu Usulu Al Kafy ,olemba Al Mazindarany 10/106).

---

Ndimalizira ndi zomwe ndinaonera ndikumvera zamushia wachirafidwy waku Egypt komanso ali m'gulu la anthu omwe anaphunzira ku Al Azhar amene amatchedwa (Hassan Shihata) mu zophunzitsa zake zimene amaphunzitsa kunja kwa Egypt, analitu akutukwana m'menemo mayi wa anthu okhulupilira Aisha (R.A) — Allah tembererani aliyense amene amazunza mayiyu ndikumamutukwana — tsopano imvani mawu ake: (1)

---------------------------------------------

(1) Ndikukupemphani kuti mukalowe website ya ''alserdaab'' ndi website ya ''Faisal Noor'' pa internet kwa amene akufuna kuonera zimenezi wokha.

• Poyankha funso loti : ''ndichifukwa ninji Aishah anatchedwa kuti Al Humayira-u? anati : Humayira-u ndikuchepetsa kwa dzina la Himarah (yemwe ndi bulu wankazi).

• Atafunsidwanso M'rafidwy ameneyu zavuto lenileni lomwe limalesa Masunni kuzindikira zoona zenizeni monga m'mene akudziwira m'rafidwy ameneyu poyankha anati: ''ndithu chiphinjo chachikulu chomwe chikwaletsa Ahlu Al Sunnah kwadziwa ma Ahlu Al Bayt ndikutsatira kwawo komutsata Aishah — anawayika bambo ake komanso Umar munyumba ya M'tumiki molanda,mwabodza komanso mwakuba. Aishah analetsa m'tembo wa imamu Al Hassan kuti uyikidwe pambali pa agogo ake, anagenda jeneza ya imamu Al Hassan ndi mivi, ndipo anati :''musalowetse m'nyumba mwanga amene ine ndimamuda, anapitiliza kulankhula — mwaukali (Shihata)— tembelero la Mulungu likhale pa iwe Aisha , tembelero la Mulungu likhale pa iwe Aisha, tembelero la Mulungu likhale pa iwe molingana ndi chiwerengero cham'pweya wazolengedwa zonse. Taona iwe mwana wa galu, Abubakar ndi Umar nkumagona munyumba ya M'tumiki, Hassan, mwana wa Al Zahraa-u (Fatwimah) ndiye kumathamangisidwa? Mukuona mavuto amene anapanga mwana wa galu. Mukuona mavuto amene anapanga wotembeleredwa ameneyu. Kodi mwana wagalu ndi ndani? Mwana wagalu anawerenga maganizo a Ummah ,ndiye anazindikira kuti ndi ummah ofooka nzeru omwenso siumakhala ndi cholinga cholozeka.

---

Ndiye ndikunena kuti: pambuyo poti ndawonetsa zikhulupiliro zamashia achi ''Imamiyyah Al Ithni Ashariyah Al Rafidhwah''amene ali Mashia aku Iran, Hizbullah, ndi ku Iraq pa azimayi a anthu okhulupilira Aishah ndi Hafswah (R.A) — ndiye sizingatheke kwa munthu amene ali ndi nzeru kuphatikizanso chipepembezo kuti aziyitanira kuchiyanjano pamodzi ndi awo amene akukhulupilira za ukafiri (kukanira) wa azimayi awokhulupilira Aishah ndi Hafswah (A.S) ndikutinso iwo anapha M'tumiki wa Allah, anayikira umboni wabodza komanso anali kugwira ntchito ya ukazitape pazochita za M'tumiki wa Mulungu.

''kuyeretsedwa konse ndi kwanu, ndithu ili ndi bodza lalikulu''

www.alburhan.com.



M'dzina la Mulungu madalitso ndi mtendere zikhale pa Mtumiki wa Mulungu. Pambuyo pake: Ambiri mwa asilamu akukhulupilira kuti palibe kusiyana muzikhulupiliro pakati pa asilamu achisunni ndi achishia komwe kungaletse kuyandikana pakati pawo, munthawi yomwe adani achisilamu mbali zonse ali kwayembekezera kuti apezane nazo zoipa asilamu.

Komanso akukhulupilira kuti Mashia ndi opambana malire,mwa iwo, akumakhulupilira zikhulupiliro zosemphana ndi chipembezo cha asilamu. Ena mwa iwo ndi apakatikati ; ili ndiye gulu la Mashia lomwe limakhulupilira zama imamu khumi ndi awiri lomwe lili lokana(limamukana Abubakar ndi Omar) awa ndiamene akufunikira kuti pakhale kuyandikana nawo mwapadera. Ndithu ku Iran dziko laima powathandizira iwowa kuchithira nkhondo chisilamu chenicheni ndi asilamu.Koma kuti kugamula kwathu pazagulu limeneli kukhale kwachilungamo tiyenera kudziwa zikhulupiliro zawo kudzera mumaphata mwawo momwe amatengera chipembezo chawo,osati kudzera muzomwe zimangonenedwa zokhudza iwowa.

Ndiye tikhala tikufotokozerana mu kakalata kathuka za chikhulupiliro cha chishia pa azimayi a okhulupilira Aishah ndi Hafsah azikazi awiri a M'neneri (S.A.W), Ndithu Mulungu anatsitsa Qur'an yomwe idzakhala ikuwerengedwa kufikira tsiku la chimaliziro,powayeretsa azimayi a anthu okhulupilira.Komanso pali mahadith ochokera kwa M'neneri (S.A.W) okhudza iwo koma kuti chishia chimakhulupilira kuti azimayi awiriwa anatuluka chisilamu ndikutinso awiriwa ndiamene anakhonza chiwembu chopha Mtumiki wa Allah ndi poyizoni(poison), amawaneneranso zoipa zina zomwe tidzitchule komwe tikupitaku.

**Choyamba: chishia chimakhulupilira kuti azimayi a anthu okhulupilira Aishah ndi Hafsah (R.A) anakufuru(anakanira) ndikuti palibe kwapatula azimayiwa mugulu lomwe linakanira pambuyo pa imfa ya M'tumiki wa Allah (S.A.W) malinga ndi chikhulupiliro chawo chabodza. Umboni wazimenezi ndizomwe ndifotokoze pansipa:**

Nkhani inachokera kwa bamboo ake a Jafar (A.S) anati :''**anthu anali atatuluka chisilamu pambuyo pa M'neneri (S.A.W)** kupatula atatu '', ndiye ndinati — oyilandira nkhaniyi — : atatuwa ndi ndani? Ndiye anati : Al Miqdad Bin Al As-wad, Abu Tharri Al Ghifaary ndi Salmaan Al Farisy''.(Rijaalu Al Kishy, P.6, Al Kaafy 8/345).

**Chachiwiri: kutemberera kwa Mashia kwatemberera azimayi a anthu okhulupilira ; Aishah ndi Hafsah (R.A)** : izitu tingazipeze mu Duwa yamafano ama Quraysh yomwe anayiyambitsa Imamu wankulu wamashia komanso m'tsogoleri wawo pochotsa boma lakale amene ali **Al Khomeiny** , yomwe amatemberera muduwa m'menemo azimayi a anthu okhulupilira Aisha ndi Hafsah (A.S) —Oh Allah tembererani amene akudana ndi awiriwa — : '' **Oh! Allah,tembelerani mafano awiri ama Quraysh,asatana awiri ama Quraysh,zopembezedwa ziwiwiri zama Quraysh,zopeka bodza ziwiri zama Quraysh,ana achikazi a awiriwa''** (Mansoor Hussein/ Tuhfatu Al Awaam Maq-bool, P.423—424).

**Chachitatu: chikhulupiliro choti ndithu amene anapha M'tumiki wa Allah (S.A.W) ndi poyizoni (poison) ndi azimayi a anthu okhulupilira Aisha ndi Hafsa (R.A) — kwayika Ayuda kukhala osalakwa**— : Nkhani inachokera kwa bambo ake a Abdullah (A.S) anati: ''Aisha ndi Hafsah tembelero la Allah likhale paiwo ndi azibambo awo Oh Mbuye wanga m'paka liti anthu amenewa adzakhala akudya matupi a anthu oopa omvera? m'pakanso liti mukhala mukwachedwetsa anthu amenewa kumavuto anu ndi kulanga kwanu? **Anthu awiri amenewatu anapha M'tumiki wa Allah ndi poyizoni''**. (Hayatu Al Quloob — Majilisy 2/700 — Edition yatsopano— Tehran).

**Chachinayi: Chikhulupiliro choti azimayi a anthu okhulupilira Aishah ndi Hafsah anali akazitape otumikira azibambo awo kunyumba ya M'tumiki wa Mulungu (S.A.W) choncho anali akufufuza nkhani za iye:**

1. Mumbali mwa buku la Salim Bin Qaysi, P.154 muli mawu oti: **ndiye anali Aisha ndi Hafsa akazitape otumikira azibambo awo** kunyumba ya M'tumiki wa Allah (S.A.W) muzochitika zonse.

2. Nkhani inachokera kwa Salim anati: ''ndinamumva Ali (R.A) akunena kuti: M'tumiki wa Allah (S.A.W) ankandisiyira mawu mutsiku lomwe adamwalira , panthawiyi m'kuti nditamuyezamitsa pachifuwa changa ndipo mutu wake unali pakhutu langa,**ndithu azimayi awiri anali atatchera makutu awo kuti adzimvetsera mawu amene adziyakhulidwa**, M'tumiki wa Allah (S.A.W) anati : Oh! Allah gonthetsani makutu a anthu awiriwa''. (Salim Bin Qaysi, P.359, mumphepete mwatsamba lake munalembedwa kuti: **amatanthauza Aishah ndi Hafsah).**

**Chachisanu: chikhulupiliro chamashia choti ndithu mayi wa anthu okhulupilira Aishah ndiamene anali kulimbikitsa zakupha khalifa Uthman Bin Affan (R.A).** Adanena Allie Bin Abi Twalib: **''Oh! Iwe Aishah dzulodzuloli wakhala ukulimbikitsa zopha Uthman** , ndikumanena kuti : ''izi ndi zovala za M'tumiki wa Allah (S.A.W) sizinasinthe , koma ndithu Uthman wasintha machitidwe (Sunnat) a M'tumiki wa Allah (S.A.W), ndiye lero ukunena zomwe ukunenazi''. (Al Idhwaahu ,Lolembedwa ndi Fadhwilu Bun Shaathaan Al Azdy, tsamba 79- (anafa m'chaka cha 260 A.H), Linawunikidwa ndi Al Sayyed Jalaalu Al Deen Al Husseiny Al Ar-mawy Al Muhaddith).

**Chachisanu ndi chimodzi: chikhulupiliri choti mayi wa anthu okhulupilira Aisha ndi m'dani wa Mulungu, m'dani wa M'tuumiki wake, komanso m'dani wa akubanja la M'tumiki wa Allah(S.A.W)** : Nkhani inachokera kwa Muhammad Bun Muslim yemwe anati: ''ndidawamva bambo a Jafar (A.S) akunena kuti munthawi yomwe amamwalira Al Hassan Bun Allie (A.S) ananena kwa Hussein kuti Eh! Iwe m'chimwene wanga, ine ndikukusiyira mawu ndiye wasunge; ngati ine ndingamwalire ndikhonzeni bwino bwino kenako ndilondolereni kwa M'tumiki wa Allah (S.A.W) kuti ndikawonane naye,kenako ndipitiseni kwamayi anga Fatimah (R.A) ndipo kenako ndibwenzeni nimukandiyika ku Baqeei, komatu dziwa kuti zindipezatu ine zoipa kuchokera kwa **''Humayira-u''** [(1)] **zinthu zomwe anthu akudziwa muzochitika zake ndi chidani chake ndi Mulungu, M'tumiki wake (S.A.W) ndi ife akubanja la M'tumiki''**.(Usulu Al Kaafy — gawo loyamba— khomo la (Al Ishaarah wa Al Nansu ala Al Hussein Bin Allie).

**Chachisanu ndi chiwiri: kukhulupilira kwa Mashia kuti azimayi a anthu okhulupilira Aishah ndi Hafsah ndithu awiriwa adamuletsa Fatwimah (R.A) kulowa m'malo muchuma cha M'tumiki(S.A.W) pogwiritsa ntchito umboni wabodza:**

Nkhani inachokera kwa Hannanu Bun Sudayir yemwe anati: Swaduqatu Bun Muslim adafunsa bambo a Abdullah (A.S) — ine ndili kwa Abdullah konko — ndiye anati :kodi mboni yoti Fatwimah asalowe m'mmalo muchuma chababmbo ake ndindani? Iye adayankha nati : **adayikira umboni ndi Aishah, Hafsah** ndi mzibambo wina ochokera mwama A'arabu (Aluya akumidzi) otchedwa Ausu Bun Al Haddathan ochokera mum'tundu wa ana a Nadir'',anayikira umboni kwa Abubakar kuti M'tumiki wa Allah (S.A.W)

-----------------------------------------

(1) Al Humayira-u : ndi dzina lomwe amamutchulira mayi wa anthu okhulupilira Aishah (R.A).(mwachipongwe) .